



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

MTENGO WA MOYO

Ndiye akunga mtengo wooka pa mitsinje ya madzi; wakupatsa chipatso chake pa nyengo yake, tsamba lake lomwe losafota; ndipo zonse azichita apindula nazo. Mastimo 1:3

Zipatso zoturuka mwa ife




Zosaoneka ndi Maso

1. Chimbolo
2. Chiyeretsa
3. Kukoma mtima
4. M'pumulo
5. Kupereka

Kufa kwa mbeu

Indetu indetu ndinena ndi inu ngati mbeu siigwa nthaka niifa ikhala payokha iyo; koma ngati ifa, ibala chipatso chambiri, iye okonda moyo wache adzautaya; ndipo odana ndi moyo m'dziko lino lapansi adzausungira ku moyo osatha **Yohane 12:24-25**



*Ine ndine M'pesa inu ndi nthambi zacke: wakukhala mwa ine, ndi ine iye ameneyo abala chipatso chambiri, pakuti kopanda ine simungathe kuchita kanthu **Yohane 15:5***



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden
Biblical

Mutu 1

MTENGO WA MOYO NDI TANTHAUZO LAKE

Mulungu anali ndi njira yothetsera imfa mwa Adam. Adam amayenera kuombedwa mwa kubadwaso (kukonzekanso), kudzera mu imfa ya mbeu. Ntchito ya Adamu ngati olima munda (**Genesis3:17-19**) Ikuonetsera choonadi cha malingaliro a Mulungu pa dongosolo lake la chipulumutso. Adamu amayenera kuzindikira kuti moyo watsopano umaturuka pomwe mbeu yakwiliridwa mu nthaka (**1Akorinto15:35-36**) chithunzithuzi ichi chikutionetsera ntchito ya chipulumutso cha Khristu mu chipangano cha kale ndi chatsopano (**John 12:24-25**) ndi kuzindikira kwa usiwa wanthu ndi kudzichepetsa komwe kumatithandiza kusendeza ku kubadwaso ku moyo watsopano. **Chithuzi #2** chikuonetsera momwe Mulungu anakonzekeretsa chilengedwe kuphuzitsa Adamu za ichi komaso tsogolo. tizakambirana bwinobwino za phata la mtengo wa moyo mu Chithuzi #2 mu chaputala 2

Pofupikitsa nkhani yokhudza chisamkho mu makhalidwe, izi zili muchidziwitso cha Mulungu cha kuti ife timasemphana ndi chifuniro chake, izi ndizo zimadziwika ngati imfa ya uzimu (**Genesis2:7**). Monga momwe Adamu analili, ifeso tikazindikira kuti ndife akufa komaso a usiwa timapatsidwa moyo. Timasandulizidwa mkuppezeka kwa Mulungu mwa mtengo wa moyo, omwe umatithekeretsa kukhala moyo wa muyaya.



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden
Biblical

Mutu 2

KUPEZA MTENGO WA MOYO NDI NYUMBA YAKE YA NZERU

Musaganize kuti ndinadza Ine kudzapasula chilamulo kapena aneneri: sindinadze kupasula, koma kukwaniritsa. Mathew5:17

Buku ili likupereka malonje a njira ya kasanthulidwe ka mau opezeka mu buku la (*Mateyu 5:17-7:29*) ndi mau othandizira a ku Deutronomo lomwe ndi buku la chisanu mu chipangano chakale. Kusanthula kwa mau uku kukugwirizana ndi (*Akolose 1:7*) *Ndipo Iye ali woyamba wa zonse, ndipo zonse zigwirizana pamodzi mwa Iye.*

Tikhala tikuona Khristu kuchokera mu zolembedwa za chipangano chakale. (Yohane 5:46) pofufuza, kugawanitsa ndi kusiyantsa. Zitionetsera kuti buku la yohane likupereka chithuzi chakuti Kristu ndiye Mbuye wa chilengedwe. Cholinga chathu kugwilitsa ntchito mitu ya nkhani yomwe ikupezeka ku mateyu 5-7 kuti tipange chimango cha maphunziro. Tebulo ili mmusiyi ikufupikitsa za zomwe tiphunzire mwatsatanetsatane.

Mateyu 5	Mateyu 6	Mateyu 7
6. Usaphe	9. Usachite umboni onama	10. Usasilire
7. Usachite chigololo	10. Usasilire	
8. Usabe		

Tebulo 1. kufupikitsa Mateyu 5-7

Kupeza Mtengo wa Moyo m'buku la Mateyu 5-7

Mateyu, Deutronomo ndi Uthenga wabwino wa Yohane ali ngati Mtengo omwe ayamba ndimfundo zapaderadera (Nthambi) koma mfundozi zimaonetsera Mphata ndi muzu Umodzi. Phata ndi muzu umeneu ndiye khristu ndi tchito yake, mu ndime imeneyi

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

Roots and fruits explained

[Sommerville, Jerry](#)



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

tikhala tikukambirana m'mene lamulo 6 kulekeza 10 a malamulo khumi kuchokera m'buku la Deutronomo akuonetseredwa bwino mu buku la Mateyu 5-7. komaso mu mutu otsatirawo tidzaonetsera momwe malamulo asanu oyambirira akukwanilitsidwaso mu ndime yomweyi ya Mateyu 5-7. malamulo asanu omalizawo akutchedwa kuti "Zipatso za malamulo khumi" ndipo asanu oyambirirawo akutchedwa kuti "Mizu ya malamulo khumi" Ndipo akupanga maziko a chimango chimenechi. Tebulo #2 Malamulo khumi mu buku la Deutronomo mofupikitsa malamulo omwe akuoneka mu Deutronomo 5 ndi Eksodo 20, mau omwe akulitsidwa mu tebulo #2 ndi zomwe tikhale tikukambirana.

Malamulo khumi (Deutronomo 5)	
Mizu	Zipatso
1. Ndinakuombolani inu chokera ku Aigiputo, musakhale nayo milungu ina	6. Usaphe
2. musazipangire Fano losema	7. Usachite chigololo
3. Musatchule dzina la Yehova pachabe	8. Usabe
4. Muzikumbukira tsiku la sabata	9. Usachite umboni onama
5. Uzilemekeza atate wako ndi amako	10. Usasilire

Tebulo #2 Malamulo khumi m'buku la Deutronomo.

Malamulowa m'buku la Mateyu 5-7 awonetseredwa mu njira izi:

1. **Kufufuza phunziro la ndime**
2. **Kugawa ndime mogwirizana ndi lamulo lililonse**
3. **Kufanizira ndime zogawidwa ndi zolembedwa m'buku la Deutronomo.**

Malamulowa ayenera kuonetseredwa mu ndondomeko.

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

Roots and fruits explained

[Sommerville, Jerry](#)

Page 4



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

Tikayang'anaso mateyu 5-7, titha kuona mu chaputala 5 iye akuvumbulutsa Malamulo atatu kuyambira lamulo 6-8, ndipo mu chaputala 6 akuvumbulutsa awiri ndiwo 9-10 mwandondomeko, ndipo caputala 7 akunena motsindika za lamulo 10.

Mwina nkumafusa kuti kodi pali phindu lanji pogwiritsa ntchito njira iyi mu kusanthula kwa mau?

1. Kupeza kunvetsetsa kwa Khristu ngati Mbuye wa mu chipangano cha kale ndi chatsopano chomwe
2. Kuonetsera kafukufuku, Kugawa Ndi Kusiyantsa Kwa Malembo
3. Kunvetsetsa kuti pali ndondomeko yomwe ikupezeka mu malembo opezeka m'buku la Mateyu 5-7 yomwe ikuthandizira kupeza, kukumbukira ndi kugwiritsa ntchito uthenga omwe ukupezeka m'menemo.
4. Kuzindikira ndondomeko yomwe ikugwirizana ndi malamulo khumi.
5. Kuyang'ana chitsanzo chomwe chikugwirizana ndi chomwe chikupezeka ku Deutronomo. Lomwe ndi buku la malamulo m'chipangano chakale (*Yohane 5:46*)
6. Kuzindikira kuti chitsanzo ichi ndi chisomo cha Khristu (Yohane 1:14)
7. Kuonetsera kuti ndime imeneyi ndi yolumikizika ndi Mtengo wa moyo opezeka ku Genesisi

Tiyeni tipange kafukufuku wathu powerenga *Mateyu 5:17-7:27* mwatsatane tsatane. Makamaka zonse pamodzi, ndime iyi ya malemba ndi yomwe tili nayo chidwi monga momwe yalembedwera m'musimu.

Musaganize kuti ndinadza Ine kudzapasula chilamulo kapena aneneri: sindinadze kupasula, koma kukwaniritsa. Pakuti indetu ndinena kwa inu, kufikira litapitirira thambo ndi dziko, kalemba kakang'ono kamodzi kapena kansonga kake kamodzi sikadzachokera kuchilamulo, kufikira zitachitidwa zonse. Chifukwa chake yense wakumasula limodzi la malamulo amenewa ang'onong'ono, nadzaphunzitsa anthu chomwecho, adzatchulidwa wamng'onong'ono mu Ufumu wa Kumwamba; koma yense wakuchita ndi kuphunzitsa awa, iyeyu adzatchulidwa wamkulu mu Ufumu



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden
Biblical

wa Kumwamba. Pakuti ndinena ndi inu, ngati chilungamo chanu sichichulukuka choposa cha alembi ndi Afarisi, simudzalowa konse mu Ufumu wa Kumwamba. *Mateyu 5:17-20*

Mateyu 5:17. Khristu akutsimikizira kuti malamulo a chipangano chakale ndi aneneri ndi olemekkezeka. Kukwanilitsidwa kwa malamulo ndicho chifukwa chokwanila cha phindu lake; komabe kuyambira ndime 19, Khristu akuonetsera kuti momwe ife tingachitire ndi malamulowa zilinso ndi zotsatira zake mu maimidwe athu a mu ufumu wake. Mwina ena nkumafusa kuti kodi Yesu ankanena malamulo ake atiwo? Sitisowekera kuyang'ana kutali kwambiri pakuti iye akulankhula za malamulo khumi omwe anaperekedwa ku Eksodo 20 komaso Deutronomo 5.

Titatha kuwerenga ***Mateyu 5: 17-7:21*** tiyambe kugawa malamulowa poyang'ana mwachindunji vesi 21 ndi 27. lamulo 6 Usaphe ndi lamulo 7 Usachite chigololo zitha kuoneka powerenga ndimezi pazokhapazokha.

Malemba a lamulo 8 la Usabe tilipitirira kaye ndipo tidzabwereranso mu chaputala ichichi.

Tsopano tipitilire ku lamulo la 9 la usachite umboni onama ndi lamulo 10 la usasilire zitha kuoneka poyang'ana mitu yomwe Khristu waikamba mu ndime ya pa Mateyu 5-7.

Kuchitira umboni onama kumakamba kwambiri za kunena bodza komaso chinyengo.

Tipeza lamulo 9 pochita kafukufuku kapena kuyang'anitsitsa Mateyu 5-7 mu chindunji cha kunena bodza ndi chinyengo ***Mateyu 6:1-2, 6:5, 6:16***, zomwe zikugwirizana ndi mafotokozeredwewa.

Yang'anirani kuti musachite zolungama zanu pamaso pa anthu kuti muonekere kwa iwo; pakuti ngati mutero mulibe mphotho ndi Atate wanu wa Kumwamba. Chifukwa chake pamene paliponse upatsa mphatso zachifundo, usamaomba lipenga patsogolo pako, monga amachita onyenga m'amasunagoge, ndi m'makwalala, kotero kuti atamandidwe ndi anthu. Indetu ndinena kwa inu, lwo alandiriratu mphotho zao.

Mathew 6:1-2



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

Ndipo pamene mupemphera, musakhale monga onyengawo; chifukwa iwo akonda kuimirira ndi kupemphera m'amasunagoge, ndi pa mphambano za makwalala, kuti aonekere kwa anthu. Indetu ndinena kwa inu, Iwo alandiriratu mphotho zao.

Mathew 6:5

Ndipo pameneponse musala kudya, musakhale ndi nkhope yachisoni, ngati onyengawo; pakuti aipitsa nkhope zao, kuti aonekere kwa anthu kuti alinkusala kudya. Indetu ndinena kwa inu, Iwo alandiriratu mphotho zao.

Mathew 6:16

Ulendo wina tidzaona lamulo 10 mu ndime zasankhidwazi, anthu okonda kwambiri chuma, adyera komaso odzikundikira chuma, sitikusowekera kuyang'ana patali pakuti mateyu 6:19 akufotokoza bwino za kudzikundikira chuma.

Musadzikundikire nokha chuma padziko lapansi, pamene njenjete ndi dzimbiri ziononga; ndi pamene mbala ziboola ndi kuba

Mathew 6:19

Mofupikitsa nkhani takwanitsa kugawa lamulo 6, 7, 9, ndi 10. Pofika tsopano mwayenera kutsimikizika za ndondomeko yopezeka ku Mateyu 5-7 tsopano poti tapeza zigawo zinayi zomwe zikukambanso za malamulo khumi tiyeni tiikeso chidwi chathu pa lamulo 8 lokuti (Usabe) ndilo lamulo lotsiriza lomwe likufotokozedwa mu ndimeyi awa ndi malemba omwe aikidwa pakati pa opanga lamulo 7 ***Mateyu 5:27*** komanso opanga lamulo 9 ***Mateyu 6:1***, iyi yayenera kukhala ndondomeko yolondola yomwe malamulowa akutsatira mu Mateyu 5-7

- Kuthetsa ukwati ndi mutu wa ***Mateyu 5:31-32***.
- Kuchita malumbiro ndi mutu wa ***Mateyu 5:33-37***
- Kuchita chilungamo ndi mutu wa ***Mateyu 5:38-48***

Kafukufuku wachangu wa malamulo khumi opezeka ku Deutronomo

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

Roots and fruits explained

[Sommerville, Jerry](#)

Page 7



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

Wina nkumayesedwa kunena kuti nkhani yothetsa ukwati pa **Mateyu 5:31-32** ikugwirizana ndi ya Usachute chigololo pa **Mateyu 5:27-30**. chodziwika bwino ndi chakuti kutha kwa banja kumapangitsa wina kuchita chigololo., koma tipeza kuti lamulo ili likulumikiza ndi Usabe, kuti tinvetsetse izi tayenera kupitanso mudongosolo la Ambuye lokhudza malamulo khumi omwe akupezeka mu buku la Deutronomo. Deutronomo amatanthuza kuti **chilamulo chachiwiri** kapena kuti **kubwerezedwa kwa malamulo**. Buku la Deutronomo lidagawidwa zigawo zomwe zimakamba za malamulo khumi, monga momwe tachitira umboni za Buku la Mateyu 5-7. Tichitiraso umboni za chigao cha ndondomeko m'buku la Deutronomo. Sikuti tichita kafukufuku komanso kugawa buku lonse la Deutronomo mu chaputala chinochi, koma tichita zokwanira kukhazikitsa malire a lamulo 7 ndi lamulo 9, bukuli. Tebulo #3 : kusiyanitsa Mateyu 5-7 ku buku la Deutronomo kuwonetsa zigawo zomwe zili ku Mateyu 5-7 ndi buku la Deutronomo. Mau okulitsidwa mu tebuloli akuonetsera pomwe zokambirana zathu zikhazikike.

Malamulo khumi	Chaputala ku Mateyu	Chaputala ku Deutronomo (mwatsatanetsatane)
1. Ndinakuombolani inu chokera ku Aigiputo, musakhale nayo milungu ina	Mateyu 5 (kutanthauzidwa)	Deutronomo 6
2. musazipangire Fano losema	Mateyu 5 (kutanthauzidwa)	Deutronomo 7
3. Musatchule dzina la Yehova pachabe	Mateyu 5 (kutanthauzidwa)	Deutronomo 8-9
4. Muzikumbukira tsiku la sabata	Mateyu 6 (kutanthauzidwa)	Deutronomo 10



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden
Biblical

5. Uzilemekeza atate wako ndi amako	Mateyu 6,7 (kutanthauzidwa)	Deutronomo 11-19
6. Usaphe	Mateyu 5	Deutronomo 19:1-22:8
7. Usachite chigololo	Mateyu 5	Deutronomo 22:9-23:15
8. Usabe	Mateyu 5	Deutronomo 23:15-25:12
9. Usachite umboni onama	Mateyu 6	Deutronomo 25:13-26:10
10. Usasilire	Mateyu 6,7	Deutronomo 26:- 28:68

Tebulo #3 kufananitsa Mateyu 5-7 ndi Buku la Deutronomo1

Kafukufuku wa changu okhudza usabe mu Deutronomo 23:15-25:12 (tebulo #3)

Kodi tingapeze bwanji poyambira pomwe ma oti Usabe akufotokozedwa mu Deutronomo? Timulola Mtumwi Paulo kuti atitsogolere mmenemo. m' buku la Akorinto 9, Paulo akubweretsa mfundo ya **Usabe** pomwe amadzikanira pankhani ya ufulu wake olandira zopereka ku Mpingo wa ku akorinto

Msilikali ndani achita nkondo, nthawi iliyonse, nadzifunira zake yekha? Aoka mipesa ndani, osadya chipatso chake? Kapena aweta gulu ndani, osadya mkaka wake wa gululo? Kodi ndilankhula izi monga mwa anthu? Kapena chilamulo sichinenanso zomwezo? Pakuti m'chilamulo cha Mose mwalembedwa, Usapunamitsa ng'ombe pakupuntha iyo dzinthu. Kodi Mulungu asamalira ng'ombe? Kapena achinena ichi konsekonse chifukwa cha ife? Pakuti, chifukwa cha ife kwalembedwa: popeza wolima ayenera kulima mwa chiyembekezo, ndi wopunthayo achita mwa chiyembekezo cha kugawana nao. Ngati takufeserani inu zauzimu, kodi nchachikulu ngati ife tituta za thupi lanu? *1Akorinto 9:7-11*



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

Mu ndime imeneyi Paulo akutenga ndime yomwe akunena kuti *Usapunamitsa ng'ombe pakupuntha iyo dzinthu* omwe akuchokera m'buku la Deutronomo 25:4 chigawo chomwecho cha Deutronomo chomwe tikufuna tichione momwe Paulo akugwiritsira ntchito mau awa akufuna kuti azipatsidwa cholowa pantchito yomwe amagwira pakati pao, akukamba izi pophatikizira onse omwe amagwira ntchito osati Ng'ombe zokha ndiye mutha kuona kuti phunziro ili likukambaso za lamulo lija la Usabe.

Kuyang'ana malire a pamwamba pa nkhani ya Usabe (tebulo #3)

Tichita kafukufuku pa nkani ya verse yotsatira pa *Deutronomo 25:4* komaso ndime yomwe ilipo tisanafike pa vesi imeneyi kuti tipeze malire a m'musi komaso pamwamba pa mutu wa Usabe m'buku la Deutronomo. Tikayang'ana ma vesi otsatira pa vesi 4 titha kuona kuti Chilungamo ndi Mutu waukulu wa *Deutronomo 25: 5-12*. mulingo onyenga ndiwo mutu waukulu wa *Deutronomo 25:13-17*, awa ndiwo malire a Usabe akupezeka pa Deutronomo 25:12 chifukwa chilungamo ndo ndondomeko yopereka zoyenera pa zochita za munthu. Umbava umachitika pomwe chilungamo sichikuperekedwa bwinobwino. Mulingo onama ndi mtundu wa chinyengo okhala nayo milingo iwiri. Wina atha kunena kuti zikugwera pa chilingamo ndi Chinyengo chomwe, koma ndime zotsatirazi *Deutronomo 25:17-18* zikukamba za chinyengo cha uchifwamba. Amaleki ankapereka chithunzuthuzi ngati zonse zili bwino koma ankayembekeza a Isiraeli adutse nayamba kupha iwo ofooka omwe amatsalira.

Kuyang'ana malire a pansu pa nkhani ya Usabe (tebulo #3)

Tsopano tikhala tikuona ndime yomwe ikupezeka tisanafike pa *Deutronomo 25:4* cholinga chathu ndi kuona malire a pomwe khani ya Usabe ikuthera ndi pomwe nkhani ya Usachite chigololo ikuyambira. Tayenera kubwela m'buyo pang'ona kufikira pa chaputala 23 pomwe mitu yokamba za Usachite chigololo. Onani Tebulo #3

nimukhale nacho chokumbira mwa zida zanu; ndipo kudzali, pakukhala inu pansu kuthengo mukumbe nacho, ndi kutembenuka ndi kufotsera chakutulukacho; popeza Yehova Mulungu wanu ayenda pakati pa chigono



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden
Biblical

chanu kukupulumutsani ndi kupereka adani anu pamaso panu; chifukwa chake chigono chanu chikhale chopatulika; kuti angaone kanthu kodetsa mwa inu, ndi kukupotolokerani. *Deuteronomo 23:13-14*

Musamapereka kwa mbuye wake kapolo wopulumuka kwa mbuye wake kuthawira kwa inu; akhale nanu, pakati panu, ku malo asankhako iye m'mudzi mwanu mwina momkonda; musamamsautsa.

Deuteronomo 23:15-16

Musamabwera nayo mphotho ya wachigololo, kapena mtengo wake wa galu kulowa nazo m'nyumba ya Yehova Mulungu wanu, chifukwa cha chowinda chilichonse; pakuti onse awiriwa Yehova Mulungu wanu anyansidwa nao.

Musamakongoletsa m'bale wanu mopindulitsa; phindu la ndalama, phindu la chakudya, phindu la kanthu kalikonse kokongoletsa.

Deuteronomo 23:18-19.

M'zera ogawira wayenera kuikidwa pakati pa *Deuteronomo 23:14 ndi 23:14* kuti tisiyanitse pakati pa Chiyero ndi kuchita chigololo mitu yochokera ku Usabe zokhudza umbava, *Deuteronomo 23:13-14* zikulumikizikandi nkhani zokhudza ukhondo, mutu wa chiyero pamene *Deuteronomo 23:15-16* akukhudzika ndi nkhani ya kunzunza akapolo moonjeza. Iyi ndi nkhani yokhudza udindo ndi umwini zomwe zikugwirizana ndi nkhani ya umbanda komaso ma vesi otsatirawa *Deuteronomo 23:18-19* akuletsa mtchitidwe wa uhule pakati pa amuna ndi akazi komaso kuika chiongola dzanja pokongozana. Mitu yoseyi yokhudza malonda ndimiyezo yokuba ndi umbanda.

Kuzindikira malire a Usabe Tebulo #3

Tsopano tafika pomwe tinakonza kuti tifike kuchokera ku Deuteronomo 25:12 taonako mitu yokamba za umbanda komaso lamulo la Usabe.

Kuzindikira malire a mkati mwa Usabe

Chinthu choyambilira koono ndi chakuti kulumbila ndi kulonjeza zikutsatiridwa ndi nkhani yokhudza kutha kwa ukwati

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

Roots and fruits explained

[Sommerville, Jerry](#)

Page 11



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

Mukawindira Yehova Mulungu wanu chowinda, musamachedwa kuchichita; popeza Yehova Mulungu wanu adzakufunsani za ichi ndithu ndipo mukadachimwako. Koma mukapanda kulonjeza chowinda, mulibe kuchimwa. *Deuteronomo 23:21-22*

Munthu akatenga mkazi akhale wake, kudzali, ngati sapeza ufulu pamaso pake, popeza anapeza mwa iye kanthu kosayenera, amlemberere kalata ya chilekanitso, ndi kumpereka uyu m'dzanja lake, ndi kumtulutsa m'nyumba mwake. Ndipo atatuluka m'nyumba mwake, amuke nakhale mkazi wa mwamuna wina. Ndipo akamuda mwamuna wachiwiriyo, nakamlemberanso kalata ya chilekanitso, ndi kumpereka uyu m'dzanja lake, nakamtulutsa m'nyumba mwake; kapena akamwalira mwamuna wotsirizayo, amene anamtenga akhale mkazi wake; pamenepo mwamuna woyamba anamchotsayo sangathe kumtenganso akhale mkazi wake, atadetsedwa iye; pakuti ichi ndi chonyansa pamaso pa Yehova; ndipo usamachimwitsa dziko, limene Yehova Mulungu wanu akupatsani likhale cholowa chanu.

Deutonomo 24:1-4

Kufananiza Deutonomo (usabe) ndi Mateyu 5-7 (Tebulo#3)

Kodi mukukumbukira kuti mutu waukulu pa *Mateyu5:31-32* ndi nkani ya kuthetsa ukwati? Ndipo kuti malumbilo ndi malonjezo ndiwo mutu waukulu wa *Mateyu5:33-37*? Chilungamo ndi mutu waukulu pa *Mateyu5:38-48*? Timasakasaka kuti kodi mitu imeneyi ili mu gulu liti? Koma tsopano tili nalo yankho Usabe. (Umbanva)

Nthambi zofanana za Deutonomo ndi Mateyu (tebulo #3)

Titha kuona kuti mitu yomweyi ikupezeka m'buku la Deutonomo komaso Mateyu 5-7. M'ndandanda ofunikawu ukupangitsa izi kusungika komaso kukumbukilika mosavuta, osatiso zokhazi koma titha kukhala ndi masanjidwe a thunthu lomwe nthambi zambiri zitha kukambidwa mkati mwa mitu yonse ikuluikulu. Tifufuza izi pambuyo tikamaliza kuumba mtengo wa kudziwa zabwino ndi zoipa kuchokera ku mau ndi malingaliro a tsiku ndi tsiku.

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

Roots and fruits explained

[Sommerville, Jerry](#)

Page 12



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

Nthambi za thunthu la Deutronomo

Kafukufuku wa tcheru wa nkhani ya Usabe, zikuonetsa kuti si nkhani ya kuba kokha yomwe ikukambidwa (mwachitsanzo **Deutronomo 24:7**) komanso kukamba motsutsana ndi kubako (kulimbikira ntchito **Aefeso4:28**) zaikidwaso pa m'ndandanda. (mwachitsanzo **Deutronomo 24:8**). mfundo izi ndi zofunika tikamaona makamaka motsutsana ndi malamulo kutsogoloku mu zokambilana zanthu monga mwaona kale kuti si mtengo wa moyo okha omwe uli ndi malamulo komaso mtengo wodziwitsa zabwino ndi zoipa.

Tiyeni tifupikitse khani yomwe timakambirana mu chaputala ichi. Tebulo #4 ikufupikitsazomwe zili mmusizi.

- (1) Tinapeza kuti pali kapangidwe komwe kakupezeka m'buku la Mateyu5-7
- (2) kapangidwe ndi chitsanzo chokhazikika mu Malamulo khumi aja.
- (3) Tinakhazikitsa mpangidwe omwe ukupezeka ku Deutronomo lomwe ndi buku la malamulonmu chipangano chakale. Mpangidwe wa mabukuwa unapezedwa kuti mu masanjidwe awa muli mitu ikuluikulu komaso mitu yothandizira
- (4) Tinapeza kuti dongosolo komaso mpangidwe zikutithandiza kupeza, kukumbukira komanso kuti tigwiritse ntchito mfundozo.
- (5) Tinapeza kuti zosiyantsa za malamulo zaikika mu mitu yaing'ono yomwe ikupezeka mu malemba.

(Mau osiyantsa opezeka ku Deutronomo mdi Mateyu.)

Mateyu chaputala 5	Mateyu chaputala 6	Mateyu chaputala 7
6. Usaphe (khalani okhululuka ndi achifundo)	9. Usachite umboni onama (funani choonadin cha uzimu)	10. Usasilire (muzikhutitsidwa)
7. Usachite chigololo (khalani oyera)	10. Usasilire (muzikhutitsidwa)	

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

Roots and fruits explained

[Sommerville, Jerry](#)



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

8. Usabe (khalani olimbika ntchito)		
----------------------------------------	--	--

Tebulo #4 : kufupikitsa ziletso za Mulungu (chifuniro cha Mulungu) Mateyu5-7

Mpangidwe ndi maziko omwe tapezawa akutithandiza kudziwa choyenera kuchita nazo izi mwa ubwino. Ndipo malemba ali mmusiwa akutiyankhira fusolo.

Chifukwa chimenechi yense amene akamva mau anga amenewa, ndi kuwachita, ndidzamfanizira iye ndi munthu wochenjera, amene anamanga nyumba yake pathanthwe; ndipo inagwa mvula, nidzala mitsinje, ndipo zinaomba mphepo, zinagunda pa nyumbayo; koma siinagwe; chifukwa inakhazikika pathanthwepo. Ndipo yense akamva mau anga amenewa, ndi kusawachita, adzafanizidwa ndi munthu wopusa, yemwe anamanga nyumba yake pamchenga; ndipo inagwa mvula, nidzala mitsinje, ndipo zinaomba mphepo, zinagunda pa nyumbayo; ndipo inagwa; ndi kugwa kwake kunali kwakukulu. *Mateyu 7:24-27*

Kufanizira Mtengo wa moyo ndi Nyumba ya nzeru

Chaputala ichi chikufotokozera za Mtengo wa moyo (chithuzi #1 cha chaputala1) ndipo chaputala chotsatirachi chikukamba za mizu ndi ya Mtengo wa moyo:

- (1) Chipulumutso
- (2) Chiyeretso
- (3) Chifuniro cha Mulungu
- (4) Mpumulo
- (5) Kupereka ndi kusamalira

Zithu izi zikuimilira chisomo cha Mulungu ndiwo phata la uthenga opezeka mu pentachuki (*mabuku asanu oyambirira a chipangano chakale*) komaso zopezeka mu chihema cha Yehova



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

Chisomo chamulungu chinaperekedwa kuti chikhale mokhalamu anthu okhulupilira kuti chitipatse ife pothawirapo mu dziko la zowawa ili, Mutu wa malembowa ndiwo MYUMBA YA NZERU, yomwe yakhazikika pa ***Mateyu 7:24-27***. Mwa njira ina zafotokozedwa kuti ndi yopapatiza pa ***Mateyu 7:13-14*** ndipo simakhala yotakata ndi zochitika za makono ano kuphatikizapo ukadaulo wa sayansi. Sungani kaye maweruzidwe anu kufikira titaona uthenga wabwino olembedwa ndi Yohane poyang'anira chifuniro cha Mulungu motsutsana ndi chifuniro cha Munthu (Mwachitsanzo kuunika ndi m'dima. ***1Yohane 1:5***)



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

MTENGO WA MOYO

Ndiye akunga mtengo wooka pa mitsinje ya madzi; wakupatsa chipatso chake pa nyengo yake, tsamba lake lomwe losafota; ndipo zonse azichita apindula nazo. Maslimo 1:3

Zipatso zoturuka mwa ife




Zosaoneka ndi Ma so

- 1. Chiombolo
- 2. Chiyeretso
- 3. Kukoma mtima
- 4. M'pumpu
- 5. Kupereka

Kufa kwa mbeu

Indetu indetu ndinena ndi inu ngati mbeu siigwa nthaka niifa ikhala payokha iyo: koma ngati ifa, ibala chipatso chambiri, iye okonda moyo wache adzautaya: ndipo odana ndi moyo m'dziko lino lapansi adzausungira ku moyo osatha **Yohane 12:24-25**



*Ine ndine M'pesa inu ndi nthambi zacke: wakukhala mwa ine, ndi ine iye ameneyo abala chipatso chambiri, pakuti kopanda ine simungathe kuchita kanthu **Yohane 15:5***

Chchithunzi #4 mtengo wa moyo ku mateyu 5-7 ndi yohane 12-17.



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

Fuso lomwe mungafuse ndi lokuti ndi chifukwa chiyani Yesu akufotokozerera malamulo asanu okha kuyambira 6kulekeza 10 ku Mateyu 5-7. Ngati malamulo alidi ofunika kwambiri ngakhale mu kaimidwe kathu ka mu ufumu wa mulungu bwanji sanafotokozerenso lamulo loyamba kufika lachisanu.

Wisdom's house ikutionetsere utumiki wathu kwa Ambuye, ngakhale izi zingaoneke ngati undende kwa ena. Ife tinamasulidwa kukutumikira Uchimo (*Yohane 8:34-36*). Mamulo asanu oyambilira aja ali mizu ya chikhulupirilo, monga momwe sitimatha kuona mizu yamtengo koma timatha kuona zipatso Yesu akutiya kuti timaudziwa mtengo ndi zipatso zake *Mateyu 7:15-19*. Malamulo asanu oyambilira aja akuimira ubale wathu ndi Khristu komanso kukhudza kwake ku miyoyo yathu ndipo ali “zithu zomwe anatchitira ife” chifukwa ife tili mwa Khristu. Zili ngati mizu ya Malamulo pomwe lamulo 6-10 omwe afotokozeredwa mu Mateyu 5-7. Tifotokozerera bwino momwe mizu ndi zipatso zikulumikizirana komaso momwe Khristu akutipatsira mamasulidwe. Chithuzi #4 chikuonetsa nthambi pamwamba komaso nthaka kusonyeza kuti ife tili obisika . Mizu mu nthaka ikuonetsera kubisika muchigawo chili nkudzachi, tikamamaliza chaputala chikudzachi tiona mwachidule buku la Yohane 12-17 lomwe likuonetsa chihema mu chipululu muja komaso mizu ya mtengo wa moyo zomwe zikuonetsa phata limodzi ndiye Khristu.



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden
Biblical

Mutu 3

Chisomo cha Mulungu ku Mateyu 5-7, ndi Yohone 12-17

Kupeza mizu mu Mtwngo wa moyo Mateyu 5-7

Mu chaputala ichi tikhala tikupeza muzu wa chipatso chilichonse pa zipatso zisanu zija kuchokera mu chaputala 2.

Muzu wa Usaphe.

Cholinga chotsogolera (muzu) cha lamulo 6 “Usaphe” “ndi Kukhululukira” ndilo dipo la kumasulidwa kwathu kuchokera ku Uchimo (Maamboledwe) Mulungu ananena pakuti ndakumasulani ku mangawa nanuso amasuleni anzanu. Tikupeza kuti tili kukumbutsidwa za maamboledwe awa kuchokera mu lamulo 1.

Ine ndine Yehova Mulungu wako amene ndinakutulutsa m'dziko la Ejipito, m'nyumba ya ukapolo. Usakhale nayo milungu ina koma Ine ndekha

Deutronomo 5:6-7

fanizo la kapolo osakhululuka uja ***Mateyu 18:21-35*** likulankhula mosabisa za kulumikizana komwe kulipo pakati pa kukhululukira ndi kukhululukidwa, komaso kufunikira kokhululukira anthu ena. Tisamafune dipo la pa mangawa chifukwa tili oyamika kwa mpulumutsi wathu yemwe anamasula ife kumangawa. Ndime iyi ya ***Mateyu 5:21-26*** ikuonetsa kuti kulephera kwathu pa kukhululukira ndi chimodzimidzi kupha.

Ku ***Mateyu 5:23-26*** ikuonetsa kuti kuima kwathu ndi oweruza kukudalira kuthekera kwathu kolongosola mangawa athu ndi athu ena.

Chifukwa chake ngati ulikupereka mtulo wako paguwa la nsembe, ndipo pomwepo ukakumbukira kuti mbale wako ali ndi kanthu pa iwe, usiye pomwepo mtulo wako kuguwako, nuchoke, nuyambe kuyanjana ndi mbale wako, ndipo pamenepo idza nupereke mtulo wako. Fulumira kuyanjana ndi mnzako wamlandu, pamene uli naye panjira; kapena mnzako wamlandu angakupereke iwe kwa woweruza mlandu, ndi

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

Roots and fruits explained

[Sommerville, Jerry](#)



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

woweruzayo angapereke iwe kwa msilikali, nuponyedwe iwe m'nyumba yandende. Indetu ndinena ndi iwe, sudzatulukamo konse, koma utalipa kakobiri kakumaliza ndiko

Mateyu 5:23-26

Muzu wa Usachite Chigololo.

Cholinga chotsogolera (muzu) cha lamulo 7 “usachite Chigololo” ndiko kukana chilichose chomwe chikupikisana ndi kutumikira Khristu, zinthu zomwe zimapikisana ndi kutumikira Khristu ndizo Mafano. Lamulo 2 kukaniza chivundi kumatchedwa chiyero kapena kudzisunga. Kukhulupirika m’banja ndi chionetsero cha kudzipereka kwathu kwa Mulungu. Mulungu anaonetsera ich m’buku la Hoseya.

Chiyambi cha kunena kwa Yehova mwa Hoseya. Ndipo Yehova anati kwa Hoseya, Muka, udzitengere mkazi wachigololo ndi ana achigololo; pakuti dziko latsata chigololo chokhachokha kuleka kutsata Yehova.

Hoseya 1:2

Tikuona Khristu kutiuzwa kuti tayenera kudzipatula ku chilichonse chomwe chingabweretse chivundi mu ulendo wathu wa uzimu Mateyu 5:29.

Koma ngati diso lako lamanja likulakwitsa iwe, ulikolowole, nulitaye; pakuti nkwabwino kwa iwe, kuti chimodzi cha ziwalo zako chionongeke, losaponyedwa thupi lako lonse mu Gehena

Mateyu 5:29

Muzu wa Usabe

Umwini komaso dzina labwino ndiwo muzu wa “Usabe” Kuba ndiko kutenga chithu ndi kuchigwiritsa ntchito popanda chilorezo cha mwini. Chikole chinkaperekedwa poopetsa

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

Roots and fruits explained

[Sommerville, Jerry](#)

Page 19



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

kuba ichi chimakhala ngati chotetezera pa mangawa omwe alipo, (*Deutronomo 24:10-14*).

Ngati wina ali nalo dzina labwino, chifuniro chabwino ndicho chimaperekedwa m'malo mwa chikole pongodzipereka ndi lumbiro. Mau oti chifuniro chabwino amagwiritsidwa ntchito kuonetsera malonda omwe akuchitika “makhalidwe a Umunthu” kuposa zomwe ali nazo, ulemu otere ndi omwe chinali chosangalatsa ndi iwo ochita nao Mlonda.

Kutchula dzina la Yehova pachabe Lamulo 3 kukuphatikizira ulemu ndi dzina labwino pokwaniritsa malonjezano ndi kudzipereka kwake, komaso kupereka mangawa ake ndiwo muzu wa Usabe. Tisapeputse kuthekera kwake komaso kudzipereka komwe ali nako pa malonjezano ake. Ndipo tisalingalire uchita umwini pa zithu zomwi iye mwini alinazo (*Mateyu 5:33-37*) ndipo tisakhale anthu osalingalira za kudzipereka kwathu kwa iye (*Mateyu 5:31-32*) pakuti ichi chimaonetsa umbava. Chitsanzo chabwino cha mfundo iyi ikupezeka *Mateyu 24:45-51*.

Muzu wa Usachite Umboni onama.

Mpumulo wa uzimu ndiwo muzu wa “Usachite Umboni onama” timakonda kukhala olimbika mtima pa maonekedwe onyenga, koma mulungu amaona zonsezo zitsanzo zonse pa zopereka, mapemphero ndi kusala kudya *Mateyu 5:2-3* zikuonetsera chikhalidwe chathu cha kudalira thupi (za kanthawi kochepe) ndipo zosezi zikupereka njira ina ku mbali ya uzimu (za muyaya) Chikhulupirilo chathu chikhazikike pa zithu zosaonekazo. Mpumulo wa Mulungu (Uzikumbukira Sabata) lamulo la 4. *Ahebri 4:9-12* akufotokoza bwino.

Momwemo utsalira mpumulo wa Sabata wa kwa anthu a Mulungu. Pakuti iye amene adalowa mpumulo wake, adapumulanso mwini wake kuntchito zake, monganso Mulungu kuzake za iye. Chifukwa chake tichite changu cha kulowa mpumulowo, kuti wina angagwe m'chitsanzo chomwe cha kusamvera. Pakuti mau a Mulungu ali amoyo, ndi ochitachita, ndi akuthwa koposa lupanga lakuthwa konsekonse, napyoza kufikira kugawira moyo

[WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021](#)

Roots and fruits explained

[Sommerville, Jerry](#)

Page 20



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

ndi mzimu, ndi zimfundo ndi mafuta a m'mafupa, nazindikiritsa zolingirira ndi zitsimikizo za mtima. Ndipo palibe cholembedwa chosaonekera pamaso pake, koma zonse zikhala za pambalambanda ndi zovundukuka pamaso pake pa Iye amene tichita naye.

Ahebri 4:9-13

Muzu wa usasilire

Kupereka ndi chisamaliro cha Mulungu ndicho muzu wa (Usasilire) chisamaliro chake chimaposa zomwe ife ngati makolo timachitira ana athu, Popeza Yehova ndiye m'busa wathu pakuti ife talandiridwa kukhala ana ake sitidzasowa kanthu (Masalimo 23:1) Uzilemekeza Atate wako ndi Amako lamulo 5 likutionetsa kuti ife si amasiye iye anatipatsa ife otiyang'anira (Makolo) atisamalire ndi kutipatsa zosowa. Tikuona kuti lamulo 5 likuonetsedwa ku Mateyu 7:1-6 ndi 7-11. Timalemekeza Atate athu a kumwamba polorera kuti chipatso chatu chituluke ku Mizu yake, tisaganize kuti tingachite kanthu popanda ulamuliro wake. Tikamakhala ngati oweruza osakhwima, tili nao maonedwe a kanthawi kochepe chabe ndipo tidzipereka ku zotsatira za chivundi (mateyu 7:1-3, Agalatiya 6:8a). Pamene zipatso zathu zichokera mu Mizu yake timaweruzwa bwino komaso kuchita molungama.(Mateyu 7:5, Agalatiya 6:8b, Yohane 7:24) ndipo timakhala omuimilira.

Ife ndi adindo chabe a Mulungu pa ana ake omwe wangotidalira nao, tili makolo aku thupi, Mulungu ali Tate wathu wa kumwanba kholo lathu yemwe amatipatsa zonse mwa ufulu. Yakobo 1:5.

Pemphani, ndipo chidzapatsidwa kwa inu; funani, ndipo mudzapeza; gogodani, ndipo chidzatsegulidwa kwa inu; pakuti yense wakupempha alandira; ndi wakufunayo apeza; ndi kwa wogogodayo chitsegulidwa. Kapena munthu ndani wa inu, amene pompempha mwana wake mkate, adzampatsa mwala? Kapena pompempha nsomba, adzampatsa iye njoka kodi? Chomwecho, ngati inu, muli oipa, mudziwa kupatsa ana anu

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

Roots and fruits explained

[Sommerville, Jerry](#)

Page 21



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden
Biblical

mphatso zabwino, kopambana kotani nanga Atate wanu wa Kumwamba adzapatsa zinthu zabwino kwa iwo akumpempha Iye?

Mateyu 7:7-11

Kufananitsa Mtengo wa Moyo ndi Deutronomo 6-19

Cholinga cha gao ili ndi kusiyanyitsa Mizu ya malamulo 1-5 ndi buku la Deutronomo. Mau okulitsudwa mu Tebulo #5 akufupikitsa zomwe tikhale tikufufuza. Mau okilitsidwa mu tebulo ndiyo mitu isanu yomwe tikambirane.

Malamulo khumi	Deutronomo (m'ndandanda wake)
1. Ndinakuombolani kuchokera ku Aigiputo, musakhale nayo milungu ina	Maomboledwe: Deutronomo 6
2. Musadzipangire milungu yosema	Mayeretsedwe: Deutronomo 7
3. Usatchule dzina la yehova pachabe	Kukoma mtima: Deutronomo 8-9
4. Uzikumbukira sabata	Mpumulo, choonadi cha uzimu Deutronomo 10
5. Uzilemekeza atate wako ndi amako	Kupereka ndi kusamalira Deutronomo 11-19
6. Usaphe	Deutronomo 19:1-22:8
7. Usachite chigololo	Deutronomo 22:9-23:14
8. Usabe	Deutronomo 23:15-25:12
9. Usachite umboni onama	Deutronomo 25:13-26:10
10. Usasilire	Deutronomo 26:11-28:68

Tebulo #5 kufupikitsidwa kwa malamulo khumi m'buku la Deutronomo.

Cholinga chathu ndi kupeza Mizu yatchulidwa m'mambayi

- (1) Maomboledwe
- (2) Mayeretsedwe
- (3) Kukoma mtima

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

Roots and fruits explained

[Sommerville, Jerry](#)

Page 22



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

(4) Mpumulo, choonadi cha uzimu

(5) Kupereka ndi kusamalira

Pofanizira buku la Deutronomo tayenera kuchita monga momwe timachitura ndime zapitazi. Kufufuza, Kugawa, ndi kufananitsa buku la Deutronomo Tingapeze bwanji lamulo loyamba M'buku la Deutronomo? Yesu anatiuza pomwe tingalipeze ku **Mariko 12:29-30**.

Yesu anayankha, kuti, La m'tsogolo ndili, Mvera, Israele; Ambuye Mulungu wathu, Ambuye ndiye mmodzi; ndipo uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse, ndi mphamvu yako yonse

Mariko 12:29-30.

Mau awa akuwatenga pa Deutronomo 6:4-5

Imvani, Israele; Yehova Mulungu wathu, Yehova ndiye mmodzi; 5ndipo muzikonda Yehova Mulungu wanu ndi mtima wanu wonse, ndi moyo wanu wonse, ndi mphamvu yanu yonse. Ndipo mau awa ndikuuzani lero, azikhala pantima panu

Deutronomo 6:4-5

Chomwe chikupatsa chidwi ndi chakuti malamulo khumi alembedwa ku **Deutronomo 5:6-21**, koma Khristu akutionetsera **Deutronomo 6:4-5** chifukwa chani? Zikupezeka kuti ma lamulo aja adawafupikitsa ku **Mateyu 5:6-21** koma anaikidwa mwa ndondomeko ku Deutronomo 6-28.

Mutha kuona ndime izi ndi kufupikitsa chabe kwa zipatso za malamulo 6-10 mu Tebulo #3 kolamu 3 mu kolamu yomweyo ya tebulo 1 tipezamo ndime yomwe ikupereka tsatanetsatane wa Deutronomo.



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

Kufufuza Maomboledwe (Tebulo #5, rolo 1)

Tapeza pomwe lamulo loyamba likupezeka ku **Deutronomo 6::4-5**. chomwe tikusowekera kuchita ndi kufufusa ndime imeneyi ngati nkhani yokhudza kulipira dipo la ufulu wathu ikupezeka (Maomboledwe) ku **Deutronomo 6:21** tikupezako nkhani yomweyi.

Akakufunsani ana anu m'tsogolomo, ndi kuti, Mbonizo, ndi malemba, ndi maweruzo, zimene Yehova Mulungu wathu anakulamulirani, zitani? Pamenepo muzinena kwa ana anu, Tinali akapolo a Farao mu Ejipito; ndipo Yehova anatitulutsa mu Ejipito ndi dzanja lamphamvu

Deutronomo 6:21

Ana a Isiraeli amayenera kuzindikira kuti Mulungu ndi yemwe anawaombola ndipo amayenera kuuza izi kuchoka m'badyo wina kufikira wina.

Kupeza lamulo loyamba kunali kosavuta m'buku la Deutronomo. Koma kuti tipeze enawa zisowekera kafukufuku poyang'ama malemba mogwirizana ndi zomwe tatanthauzira ku Mateyu 5-7 komaso ku **Deutronomo 5:6-21**. Zithu zisanu zija zomwe tafotokozera kale zikupereka tanthauzo lomveka bwino. Ndizo:

1. Maomboledwe
2. Mayeretsedwe
3. Kukoma mtima
4. Mpumulo, choonadi cha uzimu
5. Kupereka ndi kusamalira



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

Kufufuza Mayeretsedwe (Tebulo #5, rolo 2)

Lamulo lachiwiri limatiuza kuti tisadzipangire milungu yosema. Tiona mwa chidwi malemba opezeka ku Deutronomo 6 kuti tipeze pomwe pakulongosoledwa zokhudza kupewa mafano (milungu yosema) akambapo za milungu ina.

Deutronomo 6:14

Musamatsate milungu ina, milungu ina ya mitundu ya anthu akuzinga inu; 15pakuti Yehova Mulungu wanu ali pakati panu, ndiye Mulungu wansanje; kuti ungapse mtima wa Yehova Mulungu wanu, ndi kukuonongani, kukuchotsani pankhope padziko lapansi

Deutronomo 6:14-15

Malingalilo awa kautionetsera Mulungu ndi wa nsanje, awa ndi malingalilo omwe tinapeza ku ***Mateyu 6:24***

Palibe munthu angathe kukhala kapolo wa ambuye awiri: pakuti pena adzamuda mmodziyo, ndi kukonda winayo; pena adzakangamira kwa mmodzi, nadzanyoza wina. Simungathe kukhala kapolo wa Mulungu ndi wa Chuma.

Mateyu 6:24

Kukhala ndi chikondi chogawika ndi chimodzimodzi kukhala m'zachinyengo, komwe ndi kuononga utumiki wathu kwa Ambuye. Kutchulidwa kwa mafano si mzera ogawira lamulo 1 (usatumikire milungu ina) ndi lamulo 2 (usazipangire milungu yosema) chifukwa izi mwanjira ina zikuonetsera mchitidwe wa ayuda pa nthawi ya m'gonero,

kuzindikira Mpulumutsi ndi maomboledwe ***Deutronomo 6:17-26*** machitidwe awa ndiofanana ndi machitidwe a Akhristu pa nthawi ya m'gonero. (***1 Akorinto 11:24-34***).



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

Mzera weniweni ogawira lamulo 1 ndi 2 ndi kusiyanitsa pakati pa ***Deutronomo 6:25, 7:1*** komaso mafano (Deutronomo 7:3-4) akufotokozerana ngati kubwera kwa mafuko asanu ndi awiri omwe anali amphanvu kuposa Isiraeli ***Deutronomo 7:1*** mafuko awa akuimilira zikhalidwe zathu za uchimo zomwe zimachita ufumu mwa ife ***Yohane 8:34*** Ngati sitinakhale moyo wathu motsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, ndiye kuti ena anatiphunzitsa makhalidwe a uchimo zomwe zikupangitsa kuti ife tikhale osowekera mayeretsedwe, kupatukana ndi kudzychotsa pakati pa anthu a m'tundu otere, kudzipatula kumene Mulungu akunena ndi kwa kudetsedwa mu uzimu osati kwa pakati pa mtundu ndi mtundu. (***Deutronomo 7:4, Yohane 8:39***), Mavuto athu amachokera m'nkati osati kunjika kwathu, (***Mariko 7:15-23***). Muchipangano cha tsopano timauzidwa za kupha makhalidwe a uchimo mwa ife.

Chifukwa chake fetsani zizalozo zili padziko; dama, chidetso, chifunitso chamanyazi, chilakolako choipa, ndi chisiriro, chimene chili kupembedza mafano

Akolose 3:5

pakuti ngati mukhala ndi moyo monga mwa thupi, mudzafa; koma ngati ndi mzimu mufetsa zochita zake za thupi, mudzakhala ndi moyo

Aroma 8:13

Mafuko asanu ndi awiri aja amaimilira zinthu zose zomwe mulungu amaletsa ana a Isiraeli kuti asachite mu malamulo khumi muja.

1. Kudzikweza
2. Kuukira
3. Kuwawa mtima
4. Kudzidetsa



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

5. Kuba

6. Chinyengo

7. Dyera

Mundu ulionse omwe ukupezeka m'buku la *Deutronomo 7:1* uli mu ndondomeko yake yogwirizana ndi zinthu zisanu tatchula pamwambazi ngati zitsanzo. Ahivi akuoneka pa nambala 6 pa m'ndandanda wa mafuko asanu ndi awiri aja, ndipo chithu chomwe chili pa m'ndandanda wa makhalidwe aja ndi Chinyengo. Ahivi (*Yoshua 9;1-22*) tizafotokozera bwino mu chaputala 5 komwe ndandanda wa zikhalidwe zija zikuchokera.

Ife sitinadziyeretsa tokha koma Mulungu ndi yemwe anatiyeretsa. Uwu ndi umboni ochokera ku chipulumutso cha Ambuye *Deutronomo 7:3*

nakawapereka Yehova Mulungu wanu pamaso panu, ndipo mukawakanthe; pamenepo muwaononge konse; musapangana nao pangano, kapena kuwachitira chifundo.

Deutronomo 7:3

Kupeza umwini ndi chifuniro chabwino cha Mulungu (tebulo 5, rolo 3)

Cholinga chathu ndiko kupeza mzera pakati pa lamulo 2 (Usadzipangile milungu yosema) ndi 3 (Usatchule dzina la Yehova pachabe) Ngati mukukumbukira kutchula dzina la Yehova pachabe kukutanthauza kuti tayenera kuzindikira umwini omwe Yehova ali nao pa zinthu zonse, komaso kuzindikira chifuniro chake chabwino ndi mbiri yabwino pokwaniritsa kudzipereka ndi kupereka dipo.

Kuyambira pa Deutronomo 8:1 sipakutenga m'ntunda kuti tipeze mau okamba za chifuniro cha Mulungu, kupereka, kukhulupirika ndi ubwino wa Mulungu.

Zovala zanu sizinathe pathupi panu, phazi lanu silinatupe zaka izi makumi anai. Ndipo muzindikire m'mtima mwanu, kuti monga munthu alanga mwana wake, momwemo Yehova Mulungu wanu akulangani inu.

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

Roots and fruits explained

[Sommerville, Jerry](#)

Page 27



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

Ndipo muzisunga malamulo a Yehova Mulungu wanu, kuyenda m'njira zake, ndi kumuopa. Pakuti Yehova Mulungu wanu akulowetsani m'dziko lokoma, dziko la mitsinje yamadzi, la akasupe ndi la maiwe akutuluka m'zigwa, ndi m'mapiri; dziko la tirigu ndi barele, ndi mipesa, ndi mikuyu, ndi makangaza; dziko la azitona a mafuta, ndi uchi; dziko loti mudzadyamo mkate wosapereweza; simudzasowamo kanthu; dziko loti miyala yake nja chitsulo, ndi m'mapiri ake mukumbe mkuwa. Ndipo mudzadya ndi kukhuta, ndi kuyamika Yehova Mulungu wanu chifukwa cha dziko lokomali anakupatsani. *Deutonimo 8:4-10*

Ambuyew akutichenjeza kuti tisatchule dzina lake pa chabe chifukwa cholephera kumuzindikira iye.

Chenjerani mungaiwale Yehova Mulungu wanu, ndi kusasunga malamulo ake, ndi maweruzo ake, ndi malemba ake, amene ndikuuzani lero lino; kuti, mutadya ndi kukhuta, ndi kumanga nyumba zokoma, ndi kukhalamo; ndipo zitachulukuka ng'ombe zanu, ndi nkhusa zanu, atachulukanso siliva wanu ndi golide wanu, zitachulukanso zonse muli nazo; mtima wanu ungatukumuke, nimungaiwale Yehova Mulungu wanu, amene anakutulutsani m'dziko la Ejipito, m'nyumba ya ukapolo.

Deutronomo 8:11-14

Chaputala 9 chikupitiliza kutichenjeza za kusalingilira chifuniro cha Mulungu, kuchita kwake ndi udindo wake wa kupezeka kwathu, pochita zikumbitso zathu kwa ife tokha.

Potero mudziwe lero lino, kuti Yehova Mulungu wanu ndiye amene aoloka pamaso panu ngati moto wonyeketsa; lye adzawaononga, lye adzawagwetsa pamaso panu; potero mudzawapirikitsa, ndi kuwaononga msanga, monga Yehova analankhula ndi inu. Musamanena mumtima mwanu, atawapirikitsa pamaso panu Yehova Mulungu wanu, ndi kuti, Chifukwa cha chilungamo changa Yehova anandilowetsa kudzaldira dziko ili; pakuti Yehova awapirikitsa pamaso panu chifukwa cha zoipa za amitundu awa. Simulowa kulandira dziko lao chifukwa cha chilungamo chanu, kapena mtima wanu woongoka; koma Yehova Mulungu wanu

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

Roots and fruits explained

[Sommerville, Jerry](#)

Page 28



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

awapirikitsa pamaso panu chifukwa cha zoipa za amitundu awa, ndi kuti akhazikitse mau amene Yehova analumbirira makolo anu, Abrahamu, ndi Isaki, ndi Yakobo. Potero mudziwe, kuti Yehova Mulungu wanu sakupatsani dziko ili lokoma mulilandire, chifukwa cha chilungamo chanu; pakuti inu ndinu mtundu wa anthu opulukira

Deutronomo 9:3-6

Titha kuona kuti nkhani yakuba ndi pamene titenga zomwe si zathu.

Kufufuza za m'pumulo (choonadi cha uzimu) [tebulo 5 rolo4]

Cholinga chathu chotsatira ndi kugawa lamulo 3 (Usatchule dzina la Yehova pa chabe) lamulo 4 (Uzikumbukira tsi sabata) cholinga cha tsiku la sabata ndiko kupewa khalidwe lokhala onyengeka ndi maonekedwe akunja chabe (zosakhalitsa) koma m'malo mwake tayenera kupumula ku ntchito zathu ndi kukhala mu Mpumulo wa Khristu (***Aheberi 4:10***)

Deutronomo 10:1 pomwe m'mzera osiyanyitsa lamulo 3 (Usatchule dzina la Yehova pa chabe) lamulo 4 (Uzikumbukira tsiku sabata) wayenera kuikidwa chifukwa ndi pomwe pakuyambira mutu wa kukumana ndi Mulungu,

Masiku aja Yehova anati kwa ine, Dzisemere magome awiri amiyala onga oyamba aja, nukwere kuno kwa Ine m'phiri umu, nudzipangire likasa lamtengo.

Deutronomo 10:1

Muchihema ndi malo omwe timakapumula mdi kukumana ndi Mulungu, Masalimo 27 ndi chitsanzo chabwino cha izi. Ansembe analibe cholowa mdziko lino, ankafunafuna chuma chazimu, ndipo ife anatitchula Ansembe achufumu mu chipangano chatsopano (***1Peturo 2:5, 2:9***) tikuona malo a mpumulo wathu ku ***Deutronomo 10:8-9***.

Masiku aja Yehova anapatula fuko la Levi, linyamule likasa la chipangano la Yehova, liimirire pamaso pa Yehova kumtumikira, ndi kudalitsa m'dzina

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

Roots and fruits explained

[Sommerville, Jerry](#)

Page 29



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

lake kufikira lero lino. Chifukwa chake Levi alibe gawo kapena cholowa pamodzi ndi abale ake; Yehova mwini wake ndiye cholowa chake, monga Yehova Mulungu wake ananena naye.

Deutronomo 10:8-9.

Likasa la chipangano limaimira kupezeka kwa Mulungu, kusiyanitsa kwa cholowa cha ku thupi ndi uzimu kukuonetsa kuti chidwi cha ansembe chinali pa zotsatira za muyaya osati za ka nthawi kochepa, Paulo anafotokozera choonadi mu Chipangano chatsopano.

Chifukwa chake sitifooka; koma ungakhale umunthu wathu wakunja uvunda, wa m'kati mwathu ukonzedwa kwatsopano tsiku ndi tsiku. Pakuti chisautso chathu chopepuka cha kanthawi chitichitira ife kulemera koposa kwakukulu ndi kosatha kwa ulemerero; popeza sitipenyenera zinthu zooneka, koma zinthu zosaoneka; pakuti zinthu zooneka zili za nthawi, koma zinthu zosaoneka zili zosatha.

2 Akolinto4:16-18

Kufufuza za kupereka ndi chisamalilo [tebulo 5 rolo 5]

Tsopano tipeze kugawa komaliza kwa pakati pa lamulo 4 (Uzikumbukira tsikula Sabata) ndi lamulo 5 (Uzilemekeza atate wako ndi amako) ngati mukukumbukira tanthauzo la kulemekeza makolo ndilo kuti tiziandira ndi kupereka chisamalilo chake. Ife ndi a dindo ake ***Deutronomo 11:3*** makolo ayenera kuphunzitsa ana awo za chisamalilo chomwe Mulungu ali nacho pa ife.

Ndipo dziwani lero lino; pakuti sindinena ndi ana anu osadziwa, ndi osapenya kulanga kwa Yehova Mulungu wanu, ukulu wake, dzanja lake lamphamvu, ndi mkono wake wotambasuka

Deutronomo11:2

Ndipo muziwaphunzitsa ana anu, ndi kuwalankhula awa pokhala inu pansu m'nyumba mwanu, ndi poyenda inu panjira, ndi pogona inu pansu, ndi pakuuka inu pomwe

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

Roots and fruits explained

[Sommerville, Jerry](#)

Page 30



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical

Deutronomo 11:19

timapezanso kuunikira kuchokera ku Mariko 7 zokhutsa lamulo 5 (Uzilemekeza atate wako ndi amako) chifukwa Yesu analankhulako izi ndi Afalisi aja za chisamarilo cha makolo ndi zakhumi.

Ndipo ananena nao, Bwino mukaniza lamulo la Mulungu, kuti musunge mwambo wanu. Pakuti Mose anati, Lemekeza atate wako ndi amai ako; ndipo iye wakunenera zoipa atate wake kapena amai wake, afe ndithu; koma inu munena, Munthu akati kwa atate wake, kapena amai wake, *Korban*, ndiko kuti Mtulo, chimene ukadathandizidwa nacho ndi ine, simulolanso kumchitira kanthu atate wake kapena amai wake; muyesa achabe mau a Mulungu mwa mwambo wanu, umene munaupereka: ndi zinthu zotere zambiri muzichita

Mariko 7:9-13

Kobani ndi liu la chiheberi lomwe linatchulidwa mu chi giliki losatanthauzidwa. Ndipo liuli likupezeka pa vesi imeneyi yokha ya ***Mariko 7:11*** liuli limatanthauza kuti Mphatso kapena icho chopatulikira Yehova, chilichonse chomwe chimatchulidwa mau awa chinali choikizidwa ku kachisi wa Mulungu, kaya ndi malo kapena chilichonse chomwe chinaikizidwa chimayenera chiomboledwe chisanafike cha maomboledwe, ***Levitiko 27:16-24***. Ambuye yesu anatsutsa afalisi aja pa chiphuzitso chonama chomwe pofuna kusunga miyambo yawo anaononga chilamulo cha Mulungu pa udindo wa ana osamalira makolo awo, kumawaphunzitsa kupereka zifukwa zoti asaperekere chisamaliro kwa makolo pomatchula mau oti Kobani pa katundu wao ndi cholinga choti amugwiritse ntchito pa zikhumitso zao.

Mu buku la Deutronomo 14 chakhumi chimayenera kugawidwa pakati pa Ansembe, amasiye andi akazi amasiye ndi ena otero, koma chomwe chinachitika ndi chakuti a Falisi anachitembenezira kwa iwo okha, ndiko kuba zomwe zikanathandiza iwo ovutika kuphatikizapo Makolo (akazi amasiye)



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden
Biblical

Koma Mlevi wokhala m'mudzi mwanu, musamamtaya, popeza alibe gawo kapena cholowa pamodzi ndi inu. Pakutha pake pa zaka zitanu muzitulutsa magawo onse a magawo khumi a zipatso zanu za chaka icho, ndi kuwalinditsa m'mudzi mwanu; ndipo abwere Mlevi, popeza alibe gawo kapena cholowa pamodzi ndi inu, ndi mlendo, ndi ana amasiye, ndi mkazi wamasiye, okhala m'mudzi mwanu, nadye nakhute; kuti Yehova Mulungu

Deutronomo 14:27-29

Mayendedwe akukhwima	Chipatso cha Malamulo (kachitidwe)	Mizu ya Malamulo (maziko)
Kuzindikira chifundo cha Mulungu ndi zosowa zathu	6. Usaphe Kumuda m'bale ndi kupha komwe, (Mateyu 5:21-26) Khalani achifundo	1. Mulungu anatiombola, timutumikire Mwachidule: Deut5:6-7 Tsatanetsatane: Mariko 12:39 Deut 6:1-24
Kuchita malingaliro a Mulungu osati athu (zokhumba)	7. Usachite Chigololo Kusilira ndi chigololonso (Mateyu 5:27-28) Kukhala osadandaula (Mateyu 5:29-30)	2. usadzipangire milungu yosema. Mwachidule: Deut 5:8-10 Tsatanetsatane: Deut 7:1-26 Mayeretsedwe: Deut 7:1-3
Kuchita mau a Yesu: osakhala okumva okha, kugwira ntchito ya uzimu ndi kuthupi komwe.	8. Usabe Kuthetsa ukwati (Mateyu 5:31,32) Kulumbira ndi Kulonjeza (Mateyu 5:33-37) Chilungamo (Mateyu 5:38-48)	3. Usatchule dzina la Yehova pachabe. Mwachidule: Deut 5:11 Tsatanetsatane: Deut 8-9 Chifuniro/ Umwini Deut 8:11-14/ 9:3-6
Kukhala owona mtima pa kufunafuna choonadi cha uzimu	9. Usachite umboni onama Chinyengo: Mu zopereka (Mateyu 6:1-40) Mu mapemphero (Mateyu 6:5-15) Mu kusala (Mateyu 6:18-18)	4. Uzikumbukira tsiku la sabata Mwachidule: Deut 5:12-15 Tsatanetsatane: Deut 10 Mpumulo Deut 10:8-9



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden
Biblical

Pamene Ambuye ndi m'busa wako ,sumasowa. (kusaka chuma chokhalitsa cha atate)	10. Usasilire Kusunga Chuma cha chivundi (Mateyu 6:19-20) Chuma chanu ndi m(M)ulingu wanu (Mateyu 6:21) Chiphamaso cha Mafano (Mateyu 6:22-24, Akolose 3:5b) Mulungu ndiye opereka (Mateyu 6:25-35)	5. Iemekeza atate wako ndi amako Mwachidule: Deut 5:16 Tsatanetsatane: Deut 11-18 kupereka, chisamaliro, Makolo Deut 11
--------------------------------------------------------------------------------------	------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------	-----------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------------

Tebulo 5: Meyendedwe akukhwima

Tebulo 2 likuonetsankuti sitinangogawa Zipatso zokha za Malamulo (6-10) komaso mizu ya Malamulo (1-5). Cholinga chathu chinali;

1. Kufufuza phunziro la ndime.
2. Kugawa ndime mogwirizana ndi lamulo lililonse.
3. Kufanizira ndime zogawidwa ndi zolembedwa mogwirizana ndi ndime zina zomwe tapeza.

Mutu 1. Tinafufuza Mateyu 5-7 kuti tione Zipatso za malamulo (6-10) mu;

Mutu 2. Tinagawa ndime kuti tionetsere mpangidwe wake ndipo tinasiyanitsa ndi izo Zolembedwa mu buku la Deutrinomo.

Mutu 3. Tafufuzaso ndime yomweyo kuti tipeze Mizu ya Malamulo (1-5) tawagawa kuti tipeze kuti pali maziko a mpangidwe uwu.